


# JOYCE MEYER

KUPHUNZIRA KUKHULUPILIRA MULUNGU  
MU NTHAWI YAKE



Liti,  
Mulungu,  
Liti?

Unless otherwise indicated, all Scripture quotations are taken from  
THE AMPLIFIED BIBLE: Old Testament.

Copyright © 1962, 1964 by Zondervan Publishing House  
(used by permission); THE KING JAMES VERSION; and from  
THE AMPLIFIED NEW TESTAMENT

Copyright © 1958 by the Lockman Foundation  
(used by permission).

Copyright © 2014 by Joyce Meyer Ministries – South Africa

All rights reserved. No part of this publication may be  
reproduced, distributed, or transmitted in any form or by any means,  
or stored in a database or retrieval system, without the prior written  
permission of Joyce Meyer Ministries – South Africa.

Joyce Meyer Ministries – South Africa  
PO Box 5, Cape Town, 8000

Phone: +27 (0) 21 701 1056  
Website: [www.joycemeyer.org](http://www.joycemeyer.org)

Go to [tv.joycemeyer.org](http://tv.joycemeyer.org) to watch Joyce's messages in a  
variety of languages

When God When? - Chewa  
Not For Resale

# ZA MKATIMU



<i>Liwu Loyamba</i>	4
1. Chikhulupiliro Ndi Nthawi	5
2. Munyengo Yake	7
3. Nyengo Yiyikika	11
4. Maitanidwe	13
5. Kudzodza	15
6. Kusiyanitsidwa (Kulekana)	21
7. Mwatopa Ndi Kudikila?	23
8. Dekhani, Chonde!	26
9. Ndiliti Limene Maloto Anga Azakwanilitsidwe?	29
Pemphero la chipulumutso	30
Za Olemba Bukhuli	31

# LIWU LOYAMBA



Tikutumikila Mulungu owona amene amatiyang'anira nthawi zonse. Mulungu sadabwitsika. Amadziwa chili conse ngakhale chinthucho chisanachitike. Masalmo 139 ikuti amadziwa malingaliro athu, ingakhale *tisanawaganizire* ndi tisanalankhule mau achokela pa kamwa pathu. Ambiri mwa ife tikuyenera kukula mbali ya chikhulupiliro, ndi kusiya kufunsa funso loti – LITI?

Chifukwa funsoli ndi lopitilira, ndalemba bukhuli kubweletsa lingaliro lomwe Mulungu wandionetsela mwa chisomo chake. Ndakhala mu moyo wanga wosaolekha ndi wokhumudwitsidwa. Kuchokela mu dzomwe ndadutsmo nazo ndaphuzira kukhulupilira modzi yeka wodziwa zonse.

Ndi pemphero langa kuti mzimu wanu ukhale ndi mtendele pamene mukupuma mwa iye ndi kukhulupilira mau a mfumu Davide, “nyengo zanga zili m'manja mwanu.” (Masalimo 31:15).

# 1



## CHIKHULUPILIRO NDI NTHAWI

“Ine ndakhulupilira Inu, ndi kudalila Inu ndinati, Inu ndinu Mulungu wanga.”

“Nyengo zanga zili m’manja mwanu, mundilanditse m’manja mwa adani anga ndi kwa iwo akundilondola ine.”

*Masalimo 31:14, 15 AMP*

Mu ndimo iyi, salimo akuti anakhulupilira Mulungu kuti amulanditse, komanso kuti achite mu nthawi yake. Kukhulupilira nkofunikila ife kulankhula “*nyengo zanga zili m’manja mwanu.*”

Ndaphunzira kuti chikhulupiliro chimafunikira ife kubvomeleza kuti mafunso ena akhala asayankhidwa ndi kuika nthawi yathu m’manja mwake – kukhulupilira kuti ingakhale tisakudziwa mayankho onse, iye akudziwa. Ali ndi nthawi yoyenela ku dzinthu zonse pa miyoyo yathu TSOPANO – *osati nthawi yina!*

Pamene tikupitiliza kukula mu moyo wathu wa chikhristu, tizaphunzira kukhulupilira kuti dzinthu zina sizingatheke pano, koma mu nthawi yoyikikayo yimene Mulungu anayikonza. Aheberi 11:1 ikuti, “Chikhulupiliro NDICHO chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, chiyesero cha dzinthu zosapenyeka.” Tikhonza kukhala nacho chikhulupiliro pano, koma sitingakhale nthawi zonse chikwanilitso chake pano.

Kukhulupilira Mulungu sikufunika kudziwa Mulungu akwanilita *bwanji*, kapena ndi *liti* limene akwanilitse. Timanena nthawi zonse, “Mulungu sachedwa,” komanso safulumila. Chifukwa chani? Chifukwa amagwiritsa ntchito mwayi *umenewo* kukulitsa chikhulupiliro chathu mwa iye. Ndipo timakula pa nthawi imene tikudikila.

M’modzi mwa abale athu amafuna chithandizo cha ndalama kuchokela kwa Mulugu kuti alipile msonkho mosayembekezela. Msonkhonowo malile ake anali pa 15 epulo. Banjali linapeleka chopeleka cha padela ku Umoyo mu Mau (Life in the Word) kukhulupilira Mulungu pa chozizwa chimene amafuna. Patafika pa 14 epulo anazipeza ndalama za msonkhozo. Mchifukwa chani nthawi zina Mulungu amadikila tsiku lomaliza?

Chifukwa ndi cha kuti akutipunzitsa ife kukhala ndi chikhulupiliro! *Chikhulupiliro sumachita kuyamwila kwa wina ayi; timaphunzitsidwa!* Timaphunzila kukhulupilira Mulungu tikadutsa mu nyengo zosiyana siyana zimene zikufunika kukhulupilira. Pakuona kukhulupilika kwa Mulungu mopitilira, tisiya kuzikhulupilira tokha, choncho timalowa mu mpumulo wa Mulungu ndi kuika chikhulupiliro chathu pa iye.

Pakuyang’ana izi, ndizophweka kuona m’mene nyengo imagwilira ntchito yopambana pophunzira kumukhulupilira Mulungu. Ngati angachite chili chonse tikufuna nthawi yomweyo, sitingakule ndi kulimba. Nthawi ndi chikhulupiliro ndi zopambona. Zimagwira ntchito limodzi.

## 2



### MUNYENGO YAKE

Levitiko 26:4 ikuti, “ndiza kupatsani mvula mu nyengo yake.” Agalatiya 6:9 (AMP) ikuti, “koma tisaleme pakuchita zabwino, pakuti pa nyengo yake tidzatuta tikapanda kufoka.” Komanso pa 1 Petro 5:6 tilimbikitsidwa “kudzichepetsa” [ife tohka] “pansi pa dzanja la mphamvu ya Mulungu kuti pa *nthawi yake* adzaticwezani” [ife tokha].

Pamene ili *nyengo yake* kapena *nthawi yake*? Ndikhulupilira kuti ndi pamene Mulungu amadziwa kuti takonzeka, pamene wina ali yense amene zikumukhuza wakonzeka ndiyenso zikugwirizana ndi dongosolo la Mulungu. Mulungu ali ndi dongosolo la wina ali yense payekha pa moyo wake, komanso ali ndi dongosolo limodzi pa dziko la pansi.

Ndimakumbukila la *nthawi* limene ndinakhumudwa chifukwa panalibe chimene chimachitika pa utumiki wanga. Ndimadziwa kuti ndadzozedwa kuphunzitsa mau a Mulungu. Komanso panalibe chitseko chimene chinatseguka, ndinaona ngati ndadikila kwa *nthawi* yayitali, ndipo ndimamva kuti ndakonzeka. Ndakhala ndikugwirizana ndi Mulungu ndipo wachita ntchito zambiri pa ine koma sindimamvetsetsa kuti ndi chifukwa chani zinthu zina sizikuchitika. Ndikukumbukila ndinamfunsa Mulungu, “Ndi chiani chimene mukudikila? Sindili wokonzeka?” Anandiyankha pakunena kuti, “Wakonzeka, koma anthu ena amene atenge mbali ndi iwe sanakonzeke, ndiponso ndikukonza zinthu zina mwa iwo, ndiye ukuyenera kuwadikilira.”

Mwaona, Mulungu samatikankhila, kutilamula, kupanga mwachinyengo kapena kukakamiza zinthu. Amatitsogolela, kutiyang'anira, kutifulumitsa ndi kuganiza. Ndi ntchito ya munthu ali yense kupeleka cholinga chake kwa iye pa chifuniro chake. Nthawi zina zimatenga nthawi kwa munthu wina koposa mzake.

Choncho, ngati Mulungu akupanga gulu la anthu amene agwilo naye ntchito limodzi, ena mwa iwo amakhala okonzeka usanafike mpumulo. Izi ndi zobvuta, kuyambira kuchibadwidwe. Samadziwa kweni kweni dongosolo la Mulungu. Ndipo nthawi zambiri samaziwana wina ndi nzake.

Chitsanzo chabwino cha ichi ndi munthu wosakwatiwa amene akupemphelera mzake wosakwatilana naye. Choncho Mulungu amamukonza munthuyo, koma amene akumpemphelelayo amatopa ndi kudikira chifukwa sadziwa chimene chikuchitika kumene kuli munthu uja. Munthu wosakwatilayu akupemphela mzake amene ali Mukhristu wokula mu uzimu. Kukula mu zipatso za Mzimu Woyera ndi kuitanidwa ku utumiki wamphumphu etc., mwina kufuna kudikila kupeza “chinthu cha padela” zonse zimakhazikika koma zimatenga nthawi, sizimangochitika. Mulungu ali ndi munthu woyenera pa iwo.

David anandipeza msanga, koma kwa iye silinali pemphelo lolamula ayi. Anamfunsa Mulungu kuti ampatse mkazi woyenelela kwa iye. Ndipo anamuza Mulungu kuti akhale munthu amene akufuna thandizo. Anapemphela kupitilira miyezi isanu ndi umodzi pakana chaka. Tinakumana nthawi zisanu, ndi tinakwatilana. Tikhala tili m'banja dzaka 28 ndipamenenso timatulutsa mbukhu ili mu 1994. Dave wakhala akunena kuti anadziwa kuti ndine woyenela usiku woyambila umene tinalo malo ena ake. Koma anadikila ndi kundifunsa ngati tingakhale limodzi chifukwa samafuna kuti ndikhale ndi mantha.

Patatha masabata atatu tili m'banja, Dave anazindikira kuti ndinali ndi mabvuto ena amene ndimafunika nao thandizo. Dave anapeza yankho lake msanga koma amayenela kupilira ku zobvuta zimene amakumana nazo pamene ndinakula mwa Ambuye, pothani ndi zobvuta zimene ndimakumana nazo masiku ambuyo.



Mulungu anadziwa kuti Dave akuyenela kuthana nazo zaka zonse zobvuta pamodzi ndi ine. Anayankhidwa mapemphelo a Dave mwa changu. Anati mu kuthekela koyenela kuthandiza munthu wina ali yense amene anali ndi mabvuto ambiri. Dave anali wofuna kuti Mulungu amugwiritse ntchito munjira imeneyi, ndipo Mulungu anamugwiritsadi ntchito. Ngati wakhala akupemphela munthu wina mokhulupilika, ndikukhulupilira kuti Mulungu wachedwelako kuyankha kufikila nthawi yoyenelekayo. Atatha Ambuye kuchita zinthu zina m'moyo wanga ndi kufika pamalo pamene Dave amafuna kuti ndifike.

Chomwe ndikufuna kunena apa ndi chokuti, pamene tikudikila pa Mulungu, tidziwe kuti Mulungu akhonza kukhala akugwira ntchito ndi anthu ena kuti pemphelo lathu liyankhidwe. Ndikukhulupilira kuti kudikila kwathu kukhale koyenera.

Tiyeni tiziganizile za *nyengo yake* poyang'ana kuonjezeledwa pa chuma. Yohane wa chitatu 2 ikuti, “Okondedwa ndikufuna pamwamba pa zonse kuti mupindule komanso kukhala ndi thanzi ngakhalenso moyo wanu upindulenso.” Pamenepa poti *moyo upindule* tiyeni tidziwe kuti kupindula kwa Mulungu kumaonekela m'makulidwe athu. *Pamene moyo wanu wapindula* zimaonetsela m'mene mungalolele kuti Mulungu abweletse malingaliro anu, zolinga zanu, ndi zochitika zikhale mu chifuniro chake. Kukula ndi ndondomeko imene imatenga nthawi. Kaya zitenga nthawi yayitali bwanji zimatengela dongosolo la Mulungu ndi m'mene tingagwirizane nalo mu dongosolo. Mulungu amatikonda kwambiri, kutipatsa ife chuma chot sitingathe kuchigwiritsa ntchito bwino. Choncho amatiuza mu Agalatiya 6:9 “Tisaleme pakuchita zabwino cifukwa mu nyengo yake tizatuta.” *Nyengo yake* ndi pamene Mulungu amadziwa kuti ndife okonzeka osati pamene tokha *tikuganiza* kuti takonzeka.

Madalitso ambiri akhonza kupangitsa munthu kuzikweza. Ndiye Baibulo ikutiwuzwa kuti sityenela kuyika munthu amene wabadwa mwatsopano pompano kukhala mtsogoleli. Chifukwa amakhala sanakule koyenela. Ndipo zikhonza kumupangitsa kuti ayambe kuzikweza (1 Tim. 3:6).

Pali nthawi ya zinthu zonse mu moyo wathu. Koma pali chitetezo pokhala m'nthawi ya Mulungu. Ndi pemphelo langa kuti ndikhale mu

chifuniro cha Mulungu ndiponso kukhala mu nthawi yake – osati kukhala patsogolo pa iye – kapena kukhala kumbuyo.

# 3



## NYENGO YIYIKIKA

Yesu anawauza ophunzira ake pa Machitidwe 1:6-8, pamene amawafunsa mafunso okhuza masiku omaliza, kuti zilibe ntchito kwa iwo kudziwa ndi nthawi yanji kapena nyengo yanji imene ili yoyenela mu masankhidwe ake ndi mphamvu yake.

Mwaona, ophunzira ake amaganiza kuti Yesu amanga ufumu padziko. Anafunsa ndiliti limene adzakhazikitse ufumu ndi kuwubweretsa ku Israyeli.

Yesu analephela kuwapanga iwo kuti amvetsetse kuti akupita kukakhazikitsa ufumu wa uzimu umene uli ufumu wa mkati mwao. Baibulo ikutichenjeza kuti chidziwitso chopanda nzeru ndi cha chabe. Zikhanakhala zopanda phindu kwa Yesu kuwauza ophunzira ake kuti ndiliti limene adzakhazikitse ufumu popeza sanamvetsetse kuti amatanthauza chiani.

Nthawi zambiri timafuna kudziwa za liti, ndipo Mulungu sangapeleke chifukwa tilibe nzeru zokwanira kugwiritsa ntchito chidziwitso. Habakuku 2:3 (AMP) ikuti “Pakuti masomphenyawo alindila nyengo yoyikidwilatu, ndipo afulumila potsilizira pake [chikwaniritso], asanama; akachedwa uwalindilire [mwa changu]; popeza afika ndithu, osazengereza.” Silizachedwa ingakhale ndi tsiku limodzi.

*Nyengo yoyikikayo* ikutanthauza pamene Mulungu akudziwa kuti

nthawi iyi ndi yoyenela. Tikuyenela kuzichepetsa tokha mu maganizo athu. Pokhulupilira mu mphamvu ndi nzeru za Mulungu akanena kuti sachedwa.

Nyengo *yoyikikayo* ikutanthauzanso kuti nthawi inakhazikitsidwa kale. Ndi kukhazikitsa pa zifukwa zina. *Zili ngati ukufuna kukumana ndi munthu.* Sitingapite pokhapokha nthawi yokumanayo itakwana, izi ndi m'mene zimayenela kukhalila. Mulungu ali ndi nyengo yoyikika, kapena tinganene kuti akufuna akumane nafe munkhazina zake za moyo wathu. Tikhonza kuzikhazikitsa pansu ndi kudikila mofatsa chifukwa zinachitika osadikila nthawi yina.

# 4



## MAITANIDWE

Nyengo imakhalapo pamene Mulungu wamuitana munthu kuti apange chinthu china chake, ndikuwadzodza kenako ndi kuwasiyanitsa kuti akagwile ntchito koma nthawi zambiri zimakhala mu njira zitatu zosiyana. Kawiri kawiri pali kutalika pa anthawi yokwaniritsa pakati pa anthu atchitowo kweni kweni ngati munthuyo agwritisidwe ntchito ndi Mulungu mu njira yeniyeni. Njira yeniyeni ikutanthauza mu njira imene ingakhuze miyoyo ya anthu ochuluka. Mu ndime ziwiri zimene zikubwelazi tiwona chimodzimodzi chochitika mu njira iyi.

Pamene Mulungu waika maitanidwe pa moyo wa munthu, chikhonza kukhala chinthu chadzidzi, kapena ohikhonza kukhala chinthu chimene munthuyo akutha kuchidziwa. Ndikumbukila kuwelenga kuti m’modzi mwa pulezidenti wa ku US anaitanidwa kukayesedwa pa nthawi imene anali wang’ono, anali ndi chikhumbokhumbo “ndikudziwa” kuti tsiku lina azakhala wasogolela ku United States.

Maitanidwe anga anabwela mwazizizi. Ndimakonza ku chipinda kwanga m’ mawa wina, ndipo liwu la Mulungu linadza kwa ine ndikuti, “Ukuyenera kupita malo onse ndi kuphunzitsa mau anga. Ndipo ukuyenera kukhala ndi maphunziro akulu a utumiki wa pamatepi.” Ingakhale sanali mau akachetechete, zinamveka mofuula ndi momveka bwino mkati mwanga. Ndipo kuyimbira pamenepo “ndinadziwa” kuti ndakhazikika, ndinali ndi chigonjetso chachikulu ndi chikhumbokhumbo chophunzitsa mau.

Sindikadziwa m'mbuyomo kuti ndinaitanidwa kuti ndikalalikile ndi kuphunzitsa mau a Mulungu. Choncho ndikayang'ana m'mbuyo mwanga ndikutha kuona zina mwa zinthuzi m'moyo wanga. Ndimakhala nthawi zonse ndi kuthekela kozionetsela ndekha polankhula ndi polemba momveka bwino. Anthu amabwela kwa ine ingakhale akusukulu ya pamwamba kuti ndiwathandize ku mavuto awo. Ndinali wokhumba kuwathandiza anthu ndi kulimbikitsa miyoyo yao. Pakana ndinafika kupeleka adiresi yakusukulu kumene ndinamalizira maphunziro anga ndi kuwapangitsa chidwi amene nadimaphunzira nao pa zinthu za zikulu. Ndinasininkhasinkha kupitanso ku sukulu kukatenga degee mu saikoloje kuti ndiwathandize anthu kuti akhale a pamwamba.

Patatha zaka zingapo tili mu banja lathu ndi Dave, ndimakula chifukwa chokhala chifupi ndi Mulungu koma ndimabvutikabe ndi mavuto osiyanasiyana m'moyo wanga chifukwa cha machitidwe anga a kale. Pano tili ndi ana atatu, ndikukumbukila pobwela kunyumba kuchokela ku tchalitchi ndinagona pa bedi usiku wa lamulungu onse atagona nyumba munali mtendere. Popanda pokhoso ndi mdima, ndinalingalila za ulaliki umene abusa amalalikila. Zimakhala ngati ndi ine amene ndinali pa guwa osati abusa ndinalibe ganizo lili lonse koma ndi chifukwa chani ndinapanga izi? Koma pano ndikudziwa.

Maitanidwe anu akhonza kubwera mwazizizi, koma pa kuyambira nthawi imene ukuitanidwa, *umakhala uli ukukonzedwa.*

# 5



## KUDZODZA

Mu nthawi yokonzedwayi, kudzodza kumamasulidwa mu nthawi yako yoyeneleka. Kudzodza ndi Mzimu Woyera umatipangitsa ife kuchita chimene Mulungu watiyitanila kuti tikachite. Mzimu Woyera umaphunzitsa, kukonza, kukwanilitsa, kuthandiza, ndi kutilimbikitsa ife. Amatikonza ndi kutipanga ife kukhala zida zoyenera kuzigwiritsa ntchito izi zikhonza kutenga zaka ndi zaka kuti zikwanilitsidwe.

Taganizani za Mose. Amamva maitanidwe pa moyo wake kuti akapulumutse anthu ake ku ziphinjo kenako anazisiya zimene amamva zija kenako ndi kupha munthu wa Aigupto amene amazonza mu Aisraeyli wina, ndiyo zasatila zake anakhala zaka makumi anai ku chipululu kuphunzira m'mene angasamalire nkhoa, kumudziwa Mulungu. Munthu wosazichepetsa sangasiyanitse kusiyana kwa kufunitsitsa ndi nthawi ya Mulungu.

Kudzodza kumapelekedwa ku miyoyo yathu molingana ndi m'mene tikupangila mu nthawi ya kutikonzekeletsa. Talingalilani za Yosefe. Anaitanidwa ndi Mulungu kuti akatsogolele ku Aigupto kupulumutsa anthu ambiri ku mabvuto. Amakhala ndi maloto a za izi m'mene anali mnyamata wachichepele. Mwa changu anawauza azichimwene ake za malotowo. Samapuma bwino bwino poganiza za nkhani yo mugwadila m'chimwene wao wang'ono, ndiyeno anamugulitsa.

Koma Yosefe samatanthauza za chowawa ayi. Anali mnyamata wa

bwino, komano sanathe kugwilitsa ntchito nzeru powauza zimene waona kumaloto. Mulungu analola zaka zimene zopweteka pamoyo wake, koma zaka zimenezi zinamupunzitsa iye kukhala ndi nzeru. Pa kupeza nzeru umakonzekela za utumiki pa moyo wake. Anadutsa mukukanidwa osati pa banja lake lokha komanso azinzake amene amakhala nao bwino, anaganiza kuti angawakhulupilire. Anamizilidwa, ndi kulangidwa pa zinthu zimene sanalakwe, ndipo anayenela kudikilira zaka zambiri asanaone kukwanilitsidwa kwa maloto ake.

Tonse timakhala tikudusana ndi zosiyanasiyana zimene zimatithandizila kukula zimatikonzekeleta kukhala moyenera ndi Mulungu ndi kukula. Mulungu samabweleta mabvuto; koma satana. Mdielekedzi amabweleta chisokonezo m'malingaliro athu. Koma Mulungu amasintha ndi kuzitemebenuza ndi kuzigwiritsa ntchito kukhala zabwino. Yosefe amadziwa izi kale chifukwa pa Genesis 50:20 anawauza azichimwene ake amene anabwela kuzalapa kuti “zimene mumazipanga kwa ine zopweteka, Mulungu anazisintha kukhala za bwino.”

Pamene Mulungu anandiyitana kukaphunzitsa mau ake, ndinali ndi banja ndi azinzanga amene anandikana ine. Ndinali ndekha ndi kupwetekedwa ndi zimenezo, ndinamizilidwa, osamvetsetsedwa ndi kulankhula za kusafunikila. Ndinali wofulumilidwa ndi wodzala ndi changu chopanda ntchito. Mwachidule *ndinadzadzidwa ndi undekha*. Ndikhonza kuonjezela ali yense pokha pokha atadusa mu njira ya kukonzeletsedwa okha.

Zikhonza kutheka kuganiza, “Osati ine – ndilibe mabvuto amenewo,” ndikhonza kunenapo kuti uli pamenepo kuzinyenga wekha! Pokha pokha “utazichepetsa” pansi pa “dzanja la Mulungu,” kuti pa nthawi yake akakukwezeni (1 Pet. 5:6).

Ndikayang'ana kumbuyo, pano ndimaona kubowoleza ku utumiki wanga zimene zikugwinzana ndi ndondomeko ya kukula kwanga ndi kudzodza kopambana.



## Maphunziro a Mau a Mulungu ku Manyumba

Choyamba Mulungu anandiuzza kuti ndisiye ntchito yolipidwa bwino kuti ndikonzekele utumiki. Chimene chinachitika chisankho ichi, chinadula ndalama zathu pakati. Mulungu anakwanilitsa zofuna zathu nthawi zonse koma nthawi zimenezo zinali zaka zophunzira.

Ndinayamba kuphunzitsa maphunziro a mau a Mulungu ku manyumba, zimene zinanditengela zaka zisanu. Pa zaka ziwiri ndi theka zoyamba, ndinapunzitsa kamodzi pa sabata. Mkumanowu unakula kenako ndiyamba kuphunzitsa kawiri – m’wawa ndi madzulo. Ingakhale ine ndi Dave nthawi imeneyi timadusana ndi mabvuto a za chuma, sindimalandila chili chonse pa mkumanowu.

Anthu amene timawaphunzitsa okwana 25 pa kukumana kuli konse, anakana ganizo la chopeleka kuti tizilandila chifukwa tinali ndi zokhumba. Zinali zobvuta kwa ine, koma zinatengela cholinga chimene ndinali nacho pomphunzitsa anthuwo. Ndinapitiliza kuphunzitsa, ndinadziwa kuti sindikuchita izi pofuna ndalama, ngakhale zinali zobvuta nthawi zina kukhala ndi mkwiyo ndi anthu, ndinaphunzila po kuti zinthu zimachitika chonchi chifukwa Mulungu sanafune kuti ndidziwe kumene kuchokele thandizolanga. Izinso zinatenga *nthawinso* pamene ndimapilila muyengo zimene ndimafuna kuthawamo.

Anthu ambili amasiya. Anaitanidwa koma chifukwa sali wofuna kupilila pamene ali mu nthawi yokonzekeletsedwa, smatha kusankha kuchokela m’maitanidwe. Mateyu 20:16 (AMP) ikuti, “Oitanidwa ndi ambriri koma osakhidwa ndi ochepa.”

Baibulo la *Amplified* linatanthauzila pa timoteo wa chiwiri 2:15 kufotokozelapo za ntchito imene tili nayo pa kuitanidwa, “Uchite changu pozionetsela kwa Mulungu wobvomelezeka (kuyesedwa). Osachita manyazi ndiponso wolunjika [kuphunzitsa bwino] nao mau choonadi.”

Mu zaka zimene tinali ndi maphunziro ku manyumba kwa anthu 25, Mulungu anandiphunzitsa zambiri zokhuza utumiki.

## **Kuikidwa pa Mbali**

Kenako, ndinakhala chaka chimodzi chimene sindinapange chili chonse mu utumiki wanga. Mulungu analankhula kwa ine, kumati, “Siyani kukumana ku manyumba; taona ndichita chinthu chatsopano.” Chikhumbokhumbo chochita maphunziro a Baibulo zapita! Ndinali ndi mwana wa khanda, ndipo chili chonse m’mtima mwanga zimandipatsa chitsimikizo ku mao ochokela kwa Mulungu.

Mu njira ina, zinali zobvuta kuti ndizilandile. Anthu anayamba kundipatsa chopeleka cha ching’ono. Nthawi zonse zimakwa pakatia pa \$15 ndi \$50. Koma zimatithandiza ife kwambiri. Ndinafunikila kusiya zonse kuti ndifike muyezo wina.

Thupi langa limayembekezera china chake kuti chichitike. Nditatha kuzipereka pakumvera, ndinakhala *chaka chimodzi popanda chochitika!* Panalibe khomo lili lonse limene linatseguka! Munjira yina, chinali chaka chobvutitsitsa m’moyo wanga. Ndinasemphana ndi Mulungu? Kodi, ndinasokoneza masomphenya anga? Zizazichitikanso? Ndingachite chiani kuti zichitikenso? Mulungu anapitiliza kulankhula nane kuti, “Khalani chete ndipo dziwani kuti ine ndine Mulungu” (Mas. 46:10).

Nthawi zina zimakhala zobvuta kuti udikile ndi kukhala mu nyengo ya Mulungu. Timakhala ndi kumvetsetsa kweni kweni kwa zinthu pamene tikuyang’ana m’mbuyo mwa zinthuzo, ndikumvetsetsa pamene tikulimbana nazo. Nthawi zina Mulungu amamwika munthu pa mbali ndi kumusiya akhala pompo. Imaoneka ngati palibe chomwe chikuchitika, komano zazikulu zimakhala zikuchitika mu uzimu. Ndi nthawi ya kukula, kuziyeletsa ndi kukhulupilira pamene palibe china chili chonse chimene tikuona.

## **Zaka Zisanu Zikubwerazi**

Pamene tikufika kumathero a chaka chodikira Dave ndi ine tinayamba kupita ku mpingo unali utangoyamba kumene kudela la St. Louis. Unali waung’ono, kunali anthu 30, koma tinali ndi umboni wa mphamvu kuti Mulungu amafuna kuti tikakhale pamenepo. Patapita nthawi,

ndinapatsidwa mwayi woyamba makumanidwe azimai m'mamawa uli wonse wa la chinai ku tchalitchi cha Life Christian Center. Maitanidwe amenewa anakonzedwa ndi Mulungu ngati mulingo wina wina wa utumika wanga, ndipo *inali nthawi ya Mulungu*.

Pamene wakukalitsa chimakula munthawi yake. Ndinakondwela ndi kubwela kwa azimai okwanila 400 pa sabata ili yonse. Ndimagwira utumiki wachinduji mu mpingo ndi kukhala otsatira wa abusa. Ndinasankhidwa kudzera ku Life Christian Center ndi kuphunzitsa college ya Baibulo. Mpingo unandithandiza ndogoso langa loyamba kutsegula radio imene imamveka ku St. Louis.

Ndinaphunzira maphunziro ofunikila mu zaka zisanu zimene ndinali kumeneko. Chimodzi chimene ndinaphunzira ndi m'mene tingazipeleke ku udindo. Munthu sali woyenela kukhala m'ndindo pakana atafika podziwa kukhala panso pa udindo. Kumbukilani kuzipeleka si kungowonetsela ntchitoyo ayi, ndi chikhalidwe. Ukhonza kusankha kuchita zimene mwauzidwa, koma chikhalidwe cha kuzipeleka chibadwe mkati mwako, makamaka ngati uli wa mphamvu ngati m'mene ndinalili.

Patapita kanthawi ndinaphunzira kugwira ntchito mu mitundu yosiyana ya utumiki. Ndinaphunziranso zambiri za kudikila. Panali zambiri zimene Mulungu anaikiza mu mtima mwanga, zinthu zoti ndichite koma kachiwirinsu, nthawi sinali yoyenela – ndiye ndinadikilanso kuphunzilanso ndi kukulanso.

Izi zinali zopambana komanso zaka zodzala ndi chimwemwe ndi misozi, zochititsa chidwi ndi zokhumudwitsa. Koma muzonsezi azibusa a Life Christian Center Rick ndi Donna Shelton, Dave ndi ine tidakali mu chinzake. Tonse takulila limodzi.

Ndaphunziranso kuti pamene anthu akulira limodzi ngati sakukhumudwitsana amakhala mu ubale wakuya umene uzakhalapo nthawi zonse. Mukhonza kunena kuti pamene kuwononga kwachoka pa iwe. Ndiye kuti wakonzedwanso.

Pamene Life Christian Center inakula kufika anthu 1,200, atsogoleri

amakonzekeletsedwa kuchoka kupita ku nyumba ya tsopano. Chili chonse chimayenda ndi chigonjetso ndi chisangalalo pamene Mulungu walankhulanso.

# 6



## KUSIYANITSIDWA (KULEKANA)

Mukumbukila pamene Mulungu analakhula kwa ine? “Maitanidwe” andifikila pamene ndimakonza ku chipinda, ndipo Ambuye anati, “Uzapita malo ena ali wonse...ndipo uzakhala ndi utmiki maphunziro a pa tepi.” Zimenezi zinakwanilitsidwa mu njira ya ying’ono mu chaka chokonzakeletsedwa, koma masomphenya anakula mu madela ena.

Tsiku lina ndikumpemphera, mau ena anandionekela a pa Afilipi 2:16 (AMP) mu njira ya mphamvu. Limati, “Kuonetsela mau kudziko (lapansi) ndi kuwapeleka kwa anthu onse Mau a Moyo...” Tsiku limeneli ndinalandila masomphenya kukafikila dziko lonse kudzela pa wayilesi.

Sindimamveka pa wayilesi ina ili yonse pamene masomphenyawa amabwela. Ndakhala ndi kuyenda yenda pang’ono koma osati kutali kutali. Munali zambiri m’mtima mwanga koma ndinapitiliza kuganiza Mulungu pena pake apanga zonse kudzela ku ntchito yanga ku Life Christian Center, chimene ndimachikonda kwambiri. Koma Mulungu anali ndi dongosolo lina.

Miyambo 16:9 (AMP) ikuti, “Mtima wa munthu ulingalira njira yake, koma Yehova ayendetsa mapazi ake.” Ndinali ndi lingaliro lomwe ndi maganizo kuti ndi dongosolo la Mulungu. Koma Mulungu anati, “Ndathana nawe pano. Tenga utumiki wako upite ku mpoto, ku mwela, ku m’wawa, ku madzulo.” Ndinaona m’zimuzi kuti ndiyenela kukhazikika makumandiwe a moyo m’mau zimene zimachitika kuchokela ku Life

Christian Center ndi kuyamba makumanidwe omwewo m’adela ena. Ndinalimbana nazo kwa nthawi yayitali koma ndinazindikila ndi Mulungu akuyanichula kuti ndichite. Ndinaziwanso kuti ngati ndalakwitsa, ndiye kuti ndataya chili chose chimene chinachitika pa zaka khumi zapitazo. Ndinamva mantha!

Kenako ndinamvera Mulungu ndi kusiya ntchito ku tchalitchi. Inali nthawi yakusintha imene Mulungu anandionetsela kuti ukundisiyanitsa ine “ku maitanidwe” a pa moyo wanga. China chili chonse chakhala chili bwino. Koma anali makonzedwe ndondomeko ili yonse mu njirayi, kud zodza kwa Mulungu kunaonjezedwa.

Pa Machitidwe 13:2 (AMP) ndipo pa “kutumikila” Ambuye iwowa, ndi kusala chakudya. Mzimu Woyera anati, “Mundipatulire (tsopano) ine Barnaba ndi Saulo ku ntchito imene ndinawayitanila.” Akhala akuchita zambiri mu utumiki, kubalal zipatso zobweletsa dalitso koma mu nthawi yake, ananena “INO ndi nthawi yoyikika.”

Ndikufuna inu mulimbikitsidwe kuti mu nyengo yake muzaona maloto ndi masomphenya amene Mulungu anatipatsa akukwaniritsidwa. Ngati wayika maitanidwe ena pa moyo wako, azakwaniritsa mu nthawi yake. Gwirizana ndi ndondomeko ndi kukumbukila kuti kuitanidwa, kud zodza ndi kusiyantsidwa kumaitanidwe kukhonza kuonekela pathata zaka zambiri. *Khalani okhulupilika mu zinthu za zing’ono. Nyengo yanu ili m’manja mwake.*

# 7



## MWATOPA NDI KUDIKILA?

Ngati mwakhala mukudikila kwa nthawi yayitali koma simukuona kuti zikupitilira mukufika, potopa kwambiri ndi kudikila. Ndikufuna ndikulimbikitseni kutenganso malingaliro ena a tsopano pa kudikila. Baibulo limati pa Marko 4:20-27, tikuyenela kukhala odikila ngati mlimi amene ayika mbeu yake pa nthaka ndi kudikila nthawi ya mvula. Mau akupitilira kunena kuti pamene akudikila kuti mbeu imele, amadzuka ndi kuikayang'ana kenako tsiku lina imaonekela. Koma milimyo samadziwa kuti yatakula bwanji.

Mulungu wandiphunzitsa kudzela ku mau awa ukhalebe mu moyo ndili nao lero pamene ndi kudikilira zinthu zimene zili mu mtima mwanga zikwanilitsidwe. Timakhala ndi zolinga pamene china chikufuna kuti chibadwe chimene sitinachisamalira ndi kusangalala ndi zinthu tili nazo.

Ndinali ndi masomphenya kuchokela kwa Mulungu zaka khumi ndisanayambe kukwanilitsidwa. Ndakhala mu zaka khumi zomwezo ndikukhlopilira ndinasemphana ndi chimwemwe chochuluka poyesa kupanga zinthu kunja kwa nthawi ya Mulungu.

Tingonena kuti mzimayi amene ali ndi ana asanu komanso ndi woyembekezelanso. Akuyembekezela kuti abeleka mwanayo mwezi woyamba. Kodi izi ndi zosatheka. Bwanji nanga atayesa kupeza kamwanako koma kumalephela kusamalila ana asanu amene alinawo? Tikhonza kuona kupusa kwa mchitidwe wonsewo, angakhale ndi

zowonadi kuti anthu amapanga choncho mu nyengo zina.

*Musangalale ndi pamene uli, pamene ukudikila kufika pamalo pamene ukufuna!* Pamene Baibulo likunena za mlimi kuti adzuka naptia ku kama lake, ndimakhulupilira kuti zimatanthauza kuti amakhala moyo umene ayenela kukhalila maziku onse pamene akuyembekezela.

Tsiku lina abusa anatinamuula pa gulu la anthu ku bwalo la ndege. Inali tsiku lotanganidwa pokwe la chikepi panali mzere, komanso malo ogula chakudya panalinso podzadza. Dzimaoneka kuti kuli konse tikupita tikungodikilira. Ndiye ndinaona kuti abusa aja anayamba kuboweka ndi zonsezi. Mwazizizi anabwela kwa ine akuti, “Ndikhulupilira kuti mukuona kuti sindidikila bwino.”

Nthawi zonse pamene sitinapunzire kudikira bwino zosatira zake zimaoneka, maganizo athu amakhala kwina, osati m'mene timakhalila machitidwe athu okha komanso thupi. Kudikila kumatenga mbali yambiri ku moyo wathu. Koma ngati kudikila nthawi zonse kumabweletsa kukhumudwa umayamba kupanika, zimene zimatenga gawo la likulu ku thupi lako ndi likhonza kubweletsa matenda. Mbusa amene sanakwanitse “kudikila bwino” anadwalapo kwambiri nthawi imeneyi ndi kufoka kwa thupi kuti mpaka adokotala ake anati zinayamba pa kanthawi chifukwa cha kupanika. *Tengani malingaliro atsopano pa kudikila, ndipo sizakhalanso zobvuta pa inu.*

Kunena mowonadi ndimakhala nthawi yayitali kudikila m'miyoyo yathu kuposa zimene timalandila. Titatha kulandila chimene timachidikila, timayambanso kudikila china. Ngati unagaone chimene ndikutanthauza utha kuzindikila mwa msanga kuti *kudikila ndi mbali yayikulu ya moyo.*

Tingonena kuti mwakwezedwa ndiye mukudikila dalitso winanso. Mukudikila kuti mukhale ndi mwana, kenako mukudikila kuti asiye kubvala thewera ndi kubvala kabudula! Kenako mukudikiranso kuti ayambe kuzigulila okha kabudula! Ukudikila kugula nyumba, kenako katundu wa nyumba mwako zimene sumaziyembekezela. Kenakonso kudikila kuyesa kupeza wantchito wokonza nyumba ndi katundu wako. Mwamvetsetsa chimene ndikutanthauza?



Phunzirani kusangalala ndi kudikila, kuzindikila kuti kudikila ndi komwe kungapeleke maloto anu. Ndikunenesa “kudikira bwino” kukwanilitsa kumachokela kwa Mulungu, koma kudikilila kuli ngati mnyamata wopekela zinthu nthawi zina munthu amayamba kudikila ndipo pamene mnyamata wopekela zinthu akufika, amapeza iye wasiya wayamba zinthu zina mwatchutchutchu szakhalaponso pa kukwanilitsa kwa zinthu zimene zija.

Anthu osadekha samatha kudikila kuti mpaka aone mathero a zinthu zazikulu chifukwa zinthu zazikulu zimatenga nthawi kuti zionekele. Mwamuna wanga, Dave, amanena nthawi zonse kuti *“zofulumila ndi sizichedwa kuonongeka; zochedwa ndi zolimba.”* Ngati zigwirizani ndi anthu osadekha ndi amene satha kudikila sizingakhaliitse. Ingakhale anthu ofuna kudikila mu nyengo ya Mulungu yoyenela, zingayikidwe pamodzi inde ndipo zizakhala kwa nthawi yayitali.

Nthawi zambiri timaona anthu akuoneka mwa changu ngati nyenyezi mu utumiki. Anthu amene amaonekela ndi kudziwika mwadzizizi pa dziko lonse nthawi zambiri. Chifukwa chimachitika ndi chakuti amakhala atadziwana ndi gulu la anthu limene linali ndi kuthekela pa kusegula makomo kapena kuoleza pa iwo. Kunena zoona utumiki wao kuhalitsa nthawi zambiri amagwa m’mbvuto a za chuma, kapena makhaliidwe chifukwa khalidwe limamangika nthawi ya kudikila. Koma iwo amakhala kuti sanaduse mukudikila nthawi yote chikhalidwe chikhazikike mwa iwo.

Anthu amene adziwika mwadzizizi ndi kusiya kudikira, nthawi zambiri, samakhala nthawi yayitali. Marko 4:5, 6 ikuti mbeu imene yatuluka mwachangu imafota pamene kutentha kwafika. Tikaphunzira kulemekeza ndi kuthokoza nthawi ya kuyembekezela, Mulungu amakhala atayamba kugwira ntchito miyoyo yathu. Ingakhale sitingaone zimene zikuchitika pakati pano, zinthu zimene zingatipangitse kukhala osangalala pano ndi zimene zimachitika kumbali pamene sitikuona.

# 8



## DEKHANI, CHONDE!

Baibulo likuti pa Ahebri 6:12 kuti timalowa mu malonjezano ake kudzela mu chikhulupiliro ndi kudheka mtima. Ndiyeno kutengelaku sikumafunika ife tichetepo kanthu ayi. Zimangofunika kudikila pakana nthawi yake yoyikikayo. Mwa chitsanzo, ukhonza kukhulupilira kapena kukhala ndi chikhulupiliro, chimene unayamwila kwa makolo ako. Koma ukuyenera kudekha kudikila nthawi yoyenera kuti ulandile. Chikhulupiliro ndi kudheka, zili pa ubale. Zimagwira ntchito limodzi ndi kubweletsa zosatila za zokhumba.

Yakobo 1:2, 3 (AMP) itiuza kusangalala “m’mene mukugwa m’mayeselo a mitundu mitundu” pozindikila kuti “chiyesedwe cha chikhulupiliro chanu” chichita chipiliro. Koma chipiliro chikhale nayo ntchito ya bwino kuti tikhale angwiro ndi opanda chirema, osasowa kanthu konse, eee! Mau a bwino!

Liwu a chiGiriki akuti “kudekha” mu ndimeyi ndi hupomone, kutanthauza kuti “kudekha kumene kumakula pamayeselo pokha.”<sup>1</sup> Mu mau ena, tingakule bwanji mu kudekha, pokha pokha tili ofuna kudikila pa chinthu chimene tikufuna kapena kupilira ku chinthu chimene sitikuchifuna pamene tikudikila?

---

1. W.E. Vine, *An Expository Dictionary of New Testament Words* (Old Tappan, New Jersey: Fleming H. Revell Co., 1940), Vol. III, p. 167

Pamene tili m'mayeselo, timakula kapena tikhonza kukula ngati tikuleka “kudekha kugwira ntchito yake yangwiro” (Yakobo 1:4). Kukana, kukhumudwa ndi kuthawa ku malo ali wonse amene ali owawa sikungabweletse kudekha. Yakobo 1:4 (AMP) ikuti tikhonza kukhala abwino ndi osasowa kanthu pamene kudekha kugwira ntchito yake bwino. Izi ndi zophweka kuona ngati munthu ali wodekha, akhonza kukhala wantendere ndi chimwemwe mu nyengo ili yonse.

Sindili wa bwino mu kudekha, koma ndakula kwambiri. Panali nthawi yina yimene ndinali munthu wosadekha, ndiponso sindimatha kudikila. Kenako ndinazindikila kuti Mulungu sazasintha, ndiye ndinaganiza kuti kuli bwino ndisinthe ndi kulowa njira yake. Ananena kuti timalandila mu chikhulupiliro ndi kudekha, choncho ndinaganiza kuti ndi bwino ndilole kudekha kukula mwa ine. *Ndakulano mu kudekha, moyenela, ndapeza mtendere ndi chimwemwe.*

Kudekha ndi chipatso cha Mzimu. Kudekha ndi umboni wa mphamvu kwa anthu wosakhulupilira. Zili ngati minofu – m'mene ukuwagwiritsa ntchito kwambiri ndi m'meneso amakhala ndi mphamvu kwabiri. Ndiyeno mukuyenera kungozipangitsa nokha kuti mukule mu kudekha – pali zinthu zina zimene sizimapangika m'mene unazinkonzela, ngati anthu ochedwa patsogolo pako, galimoto yowonogeka pa mseu, osamvetsetsa chimene chikuchitika pa moyo wako kapena kufuna yankho limene likuchedwa kubwera.

Zinthu zonsezi zimatithandizira ku mapeto, ingakhale zinali zobvuta m'mene timadusamo. Ngati tingaone izi zikhonza kutipangitsa kuyamikila za kudekha. Ahebri 12:1 (AMP) ikutilimbikitsa kuti “Tiyeni, tithamange mwa chipiliro ndi mwa makani adatiyikila ndi kupenyelela woyambira ndi womalizira.” Mpikisano uli wonse uli ndi mathelo, umadutsa pothela pa layini. Koma Ahebri watiuza m'mene tingathamangire mpikisano.

## **Kudekha kwa Iwe Mwini**

Mundilole ndikulimbikitseni inu ndi kuyamba kumanga maziko a kudekha pa moyo wanu pa kukhala wodekha ndi iwe mwini. Pamene tasokoneza,

landilani chisomo kuchokela kwa Mulungu, pitilizani pakana umathelo. Kudekhela ku iwe mwini pamene tikugonjetsa kufoka kwathu. *Kusadekha kumabweltesa kukhumudwa*, ndipo kukhumudwa kumatipititsa ku chitidwe umene uli wosakhazikika, kenako zimatipangitsa kulakwitsano kwambiri kuti ngati tingazipatse tokha kudekha kukhala poyamba m'moyo wathu.

Anthu amasintha mwa changu mu kudekha kuposa kuchiphinjo! Khalani abwino ndi kudekha. Pelekani mwaulele kwa iwe mwini ndi anthu ena. Muzapeza phindu la bwino. Luka 8:15 (AMP) ikuti “Balani zipatso ndi chipiliro.”

# 9



## NDILITI LIMENE MALOTO ANGA AZAKWANILITSIDWE?

Maloto anu adakali njira kuti awonekele! Akakali kuphikidwa munamvapo mau awa, phika woyang'anira sutentha. Ndikulimbikitsani kuti muziyesera pa tsiku lili lonse kupanga mbali yanu osati kupanga mbali ya Mulungu.

Pali nthawi yoyikika yake ya Mulungu amadziwa nthawi yake yeni yeni. Mulemekezeni Mulungu pomukhulupilira iye pamene mukadali kuyenda pa ulendo wokwanilitsidwa, *sangalalani ndi ulendo wanu!*

Palibe wina angakuuzeni ndi liti limene yankho lanu lingabwere, koma tsimikizikani lizabwera.

*Khulupilirani, ndipo lowani mu mpumulo wa Mulungu!*

# PEMPHERO LA CHIPULUMUTSO



Mulungu amakukondanani ndipo akufuna kuti kukhale pa ubale wabwino. Ngati simunamulandire Yesu ngati mpulumutsi, mukhoza kumulandira tsopano. Tsekulani mtima wanu kwa Yesu ndi kupemphera pemphero ili....

*“Atate ndikudziwa ndakuchimwirani, mundikhululukire. Ndisambitseni. Ndikulonjeza kukhulupilira Yesu mwana wanu. Ndikukhulupilira anandifera – ananyamula machimo anga pamene anafa pa mtanda. Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndikupereka moyo wanga kwa iye tsopano.*

*Zikomo atate chifukwa cha mphatso ya chikhulukiro ndi moyo wosatha. Ndithandizeni kukhala moyo wa inu mdzina la Yesu, amen.”*

Monga momwe mwapempera mu mtima mwanu, Mulungu wakulandirani, wakuyetsani ndikumatulani ku ndende ya imfa ya uzimu. Pezani nthawi ndikuwerenga mawu awa ndikufunsa Mulungu akulankhuleni pamene mukuyenda naye mmoyo watsopanowu.

Yohane 3:16

1 Akorinto 15:3 -4

Ayefeso 1: 4

Ayefeso 2: 8 – 9

1 Yohane 1: 9

1 Yohane 4: 14 – 15

1 Yohane 5:1

1 Yohane 5: 12 – 13

Pempherani kuti Yesu akuthandizeni kupeza mpingo wophunzitsa ndi kukhulupilira Baibulo kuti mulimbikitsidwe ndikukula muchiyanjano ndi Yesu Christu. Mulungu alinanu nthawi zonse akutsogolerani tsiku ndi tsiku ndipo akuwonetsani mmene mmene mukhalire mmoyo watsopano!

# ZA OLEMBA BUKHULI



JOYCE MEYER wakhala akuphunzitsa Mau a Mulungu kuyambira 1976 ndiponso mu utumiki wamphumphu kuyambira 1980. Iyeyu ndi munthu amene mabukhu ake agulitsidwa kwambiri oposela makumi asanu ndi awiri. Kuphatikizo mabuku awa *Kubvomeleza Kufunafuna Kupeza Mtendere (Approval Addiction in Pursuit of Peace)*, *Tingamvetsele Bwanji kwa Mulungu (How to Hear from God)*, ndi *Malo a Nkhondo M'malingaliro (Battlefield of the Mind)*. Watulutsanzo mazana mazana a makaseti omvotsela komanso kosungilako ma vidiyo kaseti. Mapologalamu a pa wayalesi ndi a pa kanema a Joyce a Kutsangalala Moyo Tsiku ndi Tsiku amaonetsedwa dziko lonse lapansi. Joyce amayendayenda madela ambiri kukatumikila. Joyce ndi mwamuna wake Dave, ali ndi ana anai akulu amene amakhala ku St. Louis, Missouri.